KUYAMIKA, KUPEMBEDZA, MATHOKOZO

Yehova, Ambuye wathu, dzina lanu liposadi nanga padziko lonse lapansi! amene mwaika ulemerero wanu pamwamba pa thambo.
Salmo 8:1

Ndinu woyenera, O Ambuye, kulandira ulemerero ndi ulemu ndi mphamvu, chifukwa mudalenga zinthu zonse, ndipo chifukwa cha chifuniro chanu ziripo, ndipo zinalengedwa.
Chivumbulutso 4:11

Pamene mulemekeza Ambuye, mukwezeni momwe mungathere; pakuti inde iye adzaposadi ndithu: ndipo pamene mumkuza iye, perekani mphamvu zanu zonse, ndipo musatope; pakuti simungathe kufika patali.
Mlaliki 43:30

Yehova ndiye mphamvu yanga ndi nyimbo yanga, ndipo wakhala chipulumutso changa; Mulungu wa atate wanga, ndipo ndidzamkweza. Eksodo 15:2

Yehova, Inu ndinu Mulungu wanga; Ndidzakukwezani, ndidzatamanda dzina lanu; pakuti wachita zodabwitsa; malangizo anu akale ndi kukhulupirika ndi choonadi. Yesaya 25:1

Atero Yehova, Wanzeru asadzitamandire ndi nzeru zake, kapena wamphamvu asadzitamandire ndi mphamvu zake, wolemera asadzitamandire ndi chuma chake; Koma iye wakudzitamandira adzitamandire m'menemo, kuti amandizindikira, nandidziwa Ine, kuti Ine ndine Yehova, wakucita cifundo, ciweruzo, ndi cilungamo, pa dziko lapansi; Yeremiya 9:23-24

Ndipo atapita masiku aja, ine Nebukadinezara ndinakweza maso anga kumwamba, ndipo nzeru zanga zinabwerera kwa ine, ndipo ndinalemekeza Wam’mwambamwamba, ndipo ndinatamanda ndi kum’lemekeza Iye amene ali ndi moyo kosatha, amene ulamuliro wake ndi ulamuliro wosatha, ndi ulamuliro wake. ufumu uli ku mibadwomibadwo; Ndipo onse okhala pa dziko lapansi ayesedwa opanda pake; ndipo iye acita monga mwa cifuniro cace m'khamu la kumwamba, ndi mwa okhala pa dziko lapansi; ndipo palibe woletsa dzanja lace, kapena wa kunena naye, Mucitanji? Tsopano ine Nebukadinezara ndikutamanda, ndi kukweza, ndi kulemekeza Mfumu ya Kumwamba, pakuti ntchito zake zonse ziri zoona, ndi njira zake ndi chiweruzo; Danieli 4:34-37

Chifukwa chakenso Mulungu adamkweza Iye, nampatsa dzina lomwe liposa maina onse; Kuti m’dzina la Yesu bondo liri lonse lipinde, la za m’mwamba, ndi za padziko, ndi za pansi pa dziko; ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Khristu ali Ambuye, kuchitira ulemu Mulungu Atate. Afilipi 2:9-11

Malekezero onse a dziko lapansi adzakumbukira nadzatembenukira kwa Yehova: ndipo mafuko onse a amitundu adzagwadira pamaso panu. Pakuti ufumu ndi wa Yehova, ndipo iye ndiye wolamulira mwa amitundu. Salmo 22:27-28

Perekani kwa Yehova, inu amphamvu inu, perekani kwa Yehova ulemerero ndi mphamvu. Perekani kwa Yehova ulemerero wa dzina lake; lambirani Yehova m’kukongola kwa chiyero. Salmo 29:1-2

Kuti ulemelero wanga ukuimbireni nyimbo zotamanda Inu, osakhala chete. Yehova Mulungu wanga, ndidzakuyamikani kosatha. Salmo 30:12

Ndidzalemekeza Yehova nthawi zonse: matamando ace adzakhala m'kamwa mwanga kosalekeza. Moyo wanga udzadzitamandira mwa Yehova: ofatsa adzamva, nakondwera. Lemekezani Yehova pamodzi ndi ine, ndipo tiyeni tikweze dzina lake pamodzi. Ndinafuna Yehova, ndipo anandimvera, nandilanditsa ku mantha anga onse. Salmo 34:1-4

Fuulirani kwa Mulungu, maiko inu nonse; Imbirani ulemerero wa dzina lake: lemekezani ulemerero wake. Nenani kwa Mulungu, Ndinu woopsa m'ntchito zanu! chifukwa cha ukulu wa mphamvu yanu adani anu adzagonjera Inu. Dziko lonse lapansi lidzagwadira Inu, nidzakuyimbirani Inu; adzayimbira dzina lanu. Sela. Salmo 66:1-4

Imbirani Mulungu, imbani zolemekeza dzina lace: mlemekezeni iye wokwera kumwamba, dzina lace, Yehova, ndipo kondwerani pamaso pace. Atate wa ana amasiye, ndi woweruza wa akazi amasiye, ndiye Mulungu mu mokhalamo wake woyera. Salmo 68:4-5

Ndidzalemekeza dzina la Mulungu ndi nyimbo, ndipo ndidzamkuza ndi chiyamiko. Salmo 69:30

Amitundu onse mudawapanga adzadza, nadzagwadira pamaso panu, Yehova; ndipo adzalemekeza dzina lanu. Pakuti Inu ndinu wamkulu, ndipo mumachita zodabwiza: Inu ndinu Mulungu, nokha. Salmo 86:9-10

Tiyeni, tipembedze ndi kuwerama: tigwade pamaso pa Yehova Mlengi wathu. Salmo 95:6

Perekani kwa Yehova, inu mabanja a anthu, perekani kwa Yehova ulemerero ndi mphamvu. Perekani kwa Yehova ulemerero wa dzina lace; lambirani Yehova m'kukongola kwa chiyero: Opani pamaso pake, dziko lonse lapansi. Salmo 96:7-9

Kwezani Yehova Mulungu wathu, ndipo lambirani pa chopondapo mapazi ake; pakuti ali woyera. Salmo 99:5

Inu ndinu Mulungu wanga, ndipo ndidzakuyamikani: Inu ndinu Mulungu wanga, ndidzakukwezani. Yamikani Yehova; pakuti Iye ndiye wabwino: pakuti chifundo chake amakhala kosatha. Salmo 118:28-29

Ndidzagwadira ndikuyang'ana Kachisi wanu wopatulika, Ndidzalemekeza dzina lanu chifukwa cha kukoma mtima kwanu kosatha ndi choonadi chanu; Salmo 138:2

Ndidzakutamandani, Mulungu wanga, mfumu; ndipo ndidzalemekeza dzina lanu ku nthawi za nthawi. Tsiku ndi tsiku ndidzakuyamika; ndipo ndidzalemekeza dzina lanu ku nthawi za nthawi. Yehova ndiye wamkulu, nayenera kulemekezedwa kwakukulu; ndi ukulu wake wosasanthulika. Salmo 145:1-3

Yamikani Ambuye. Lemekeza Yehova, moyo wanga. Ndidzalemekeza Yehova pokhala ndi moyo; Salmo 146:1-2

Chilichonse chokhala ndi mpweya chitamande Yehova. Y amikani Ambuye. Salmo 150:6